

LIU LA NAMIKANGO

Namikango Mission

Volume 19(1), June 2019



Kukonda Mulungu kapena Mnansi Wanga?

Ganizirani kuti mukuyenda mumsewu lero, kupita kumsika, ndipo munthu wachilendo wayamba kucheza nanu. Patatha mphindi zochepa mukucheza, mlendoyu wadziwa kuti ndinu m'Khristu. Mlendo uja kenako akuti, “Chonde, tandiuzani zimene Baibulo limanena?” Yankho lanu lingakhale lotani? Mungafotokozere bwanji mwachidule Baibulo lonse mu mphindi zochepa kwa munthu wachilendo amene sanawerengepo ndi gawo limodzi mkomwe?

Tsiku lina, Yesu amaphunzitsa gulu la anthu pamene a Farisi anabwera kwa iye kudzamufunsa. Iwo anali osakondwera ndi ziphunzitso zake, ndipo amafuna apeze njira yomukolera Yesu. Ndiye m'modzi wa iwo anali katswiri wa malamulo ndipo anamufunsa funso, “kodi lamulo lalikulu mu chilamulo ndi chiyani?” Ili likhoza kuoneka ngati funso losavuta. Koma, uwu unali msampha waukulu pa Yesu. Chilamulo cha Chiyuda chinali ndi malamulo oposa mazana asanu ndi limodzi (600), ndipo lamulo lililonse limatengedwa lofunikira kwambiri. Ngati Yesu akanasankha lamulo limodzi pamwamba pa lina, akanakhala akunena kuti malamulo ena ndi ofunika kwambiri kuposa ena. Afarisi anaganiza kuti funso lawo linali lochenjera kwambiri.

Pamenepo Yesu anayankha pompo kuti, “Udzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako onse, ndi moyo wako onse ndi nzeru zako zonse. Ili ndilo lamulo lalikulu ndi loyamba. Ndipo lachiwiri ndi ili, Udzikonda mnansi wako monga udzikonda iwe mwini” Posazengereza, Yesu anati, lamulo loyamba ndi kukonda Mulungu, ndipo lachiwiri ndi lamulo lofanana nalo ndi kukonda mnansi wako! Kenako Yesu ananena chinthu chinachake chovuta kumvetsa. Iye anati, “Malamulo onse ndi aneneri zakhazikika pa malamulo awiriwa.”

M'mau ena, Yesu anati chilamulo chonse, malamulo onse, chiphunzitso chilichonse, mu Buku Lopatulika chikhoza kuikidwa m'malamulo awiri, udzikonda Mulungu ndi mnansi wako!

Mu Liu lino tiona malamulo awiri amenewa kwambiri kuti tione zimene zili zofanana mwa iwo. Funso loyamba likufunsa funso, “Kodi mnansi wanga ndani?” Phunziro lachiwiri likuona kuti n'chifukwa chiyani tikuyenera kukonda mnansi wathu. Ndi mfundo ziwiri zimenezi, tikuyenera kudzifunsa tokha m'mene timakhalira m'madera mwanthu ndi kukondana komanso kusamalirana wina ndi mnzake kudzera mu chuma chathu pofuna kukwaniritsa chikondi cha Mulungu. Pamene mukuwerenga maphunzirowa, kumbukirani kuti Yesu akuti chilichonse mu Baibulo, chilichonse chimene ifeyo ngati a Khristu timakhulupilira, zikuima pa malamulo awiriwa, kukonda Mulungu ndi kukonda mnansi wako. Kwa a Khristu, ichi chikuyenera kukhala cholinga cha miyoyo yathu chenicheni!

Za chitukuko

Pokhala ife akhristu, timakhala ndi zosowa zosiyana siyana zomwe zimafuna ndalama. Ndipo zinthu zina zikatigwera mwadzidzidzi timasowa kokabwereka ndalama chifukwa mwina sitinathe kukonzekera posunga ndalama. Pa chifukwa ichi, Namikango Mission, kunzera mu mnthambi yake yoona za chitukuko, inayamba kuphunzitsa magulu osunga ndikubwereketa ndalama (VSL) kuti azipanga zinthu zao mwandondomeko zabwino. Kutsogoloku tikhala tikukambirana za momwe maguluwa akugwilira ntchito yake potukula miyoyo ya anthu pa chuma.
-Eric Gephart

Pofuna kuti awerengi athu amvetse bwino phunziroli, tatenga mau ambiri mu Chichewa cha lero chopezeka mu Buku loyera (Copyright 1988 by The Bible Society of Malawi).

Pitani, Mukakonde Mnansi Wanu

Werengani Luka 10:25-37

Katswiri wa chilamulo anafunsa Yesu kuti, “Ndichite chiyani kuti ndilandire moyo wosatha?” M’chilankhulo cha Chigiriki, chimene Chipangano Chatsopano chinalembedwera, ndime 25 ya Luka Mutu 10, mau akuti, ‘kuti ndilandire,’ akupitirira kufotokoza, ‘*kuti ndilandire cholowa cha moyo wosatha*’ Zinthu ziwiri zoti tizizindikire apa. Choyambirira, kodi *cholowa* ndi chiyani? Kodi chimenechi ndi chinthu chimene umachigwirira ntchito? Kodi ukhoza *kuchita* chinachake kuti upeze *cholowa cha moyo wosatha*? Kapena ndi mphatso? Ndi mphatso, Eya? Makolo akamwalira, kodi malo amakolowo amapatsidwa kwa inu kapena mumayenera kulipira? Tsopano katswiri wa chilamuloyu akuti kodi ndichite chiyani kuti ndipeze cholowa cha moyo wosatha, tikuyenera kuzindikira kuti pali vuto ndi funso limeneli.

Chachiwiri, *moyo wosatha*. Kodi zikutanthauza chiyani? Inali njira yofotokozerera za moyo uli mkudza, kapena ufumu wa kumwamba monga Yesu amakambira. Ayuda amayembekezera kuti pamene Mesiya adzabwera ndi kukonza zinthu zonse kukhala zabwino ndi kuwamasula ku kuponderezedwa kuchoka kwa a Roma, ndiye kuti nthawi yatsopano idzayambika – nthawi ili mkudza.

Yesu akuyankha osati pakupereka yankho, koma ndi funso ndipo akumufunsa kuti iye akuganiza kuti angapange chiyani. Iye akuti udzikonda Mulungu komanso mnansi wako. Yesu kenako akuti, “Yankho labwino. Ngati utachita izi, udzakhala bwino.” Yankho la munthuyu linali labwino. Mu Mateyu 22:34-30, tikuona Yesu akupereka yankho lomwelo ku funso limeneli; Konda Mulungu, konda mnansi wako iwe (Onaninso Mateyu. 7:12).

Koma mukuona chimene chinachitika pamene? Munthuyu anafunsa funso la m’mene angapezere chinthu chinachake *mitsogolo*, ndipo Yesu akumuuzza za m’mene angakhaliwe *panopa*. Izi ndi zofunikira kwambiri. Tibwereranso ku zimenezi.

Munthuyu sakukhutitsidwa, ndipo akuti amafuna “kudzipanga yekha kukhala olungama”. Tikuona funso loyamba la munthuyu, ndipo ndikufotokozerera kumeneku pazimene amachita munthu uyu akukhulupilira kuti kupeza “moyo wosatha” ndi chinthu chimene angachipeze pakuchita kwake. Iye “amayesanso” Yesu, ndipo mwina sakukonda kuti Yesu “anapambana” pazokambiranazo, ndiye akuti, “Chabwino, Ndingathe kukonda Mulungu komanso mnansi wanga. Koma ndisanamukonde, Ndikuyenera kumudziwa mnansi wangayo kuti ndindani.”

Panali mitsutso yambiri yokhudza kuti kodi mnansi wanga *ndindani* kwenikweni? Mukawerenga Levitiko 19:18, pamene lamulo lakukonda mnansi

Luka 10:25-28

Ndipo taonani, wachilamulo wina anaimirira namuyesa Iye, nanena, Mphunzitsi, ndidzalowa moyo wosatha ndi kuchita chiyani? Ndipo anati kwa iye, M’chilamulo mulembedwa chiyani? Uwerenga bwanji? Ndipo iye anayankha nati, Uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi mphamvu yako yonse, ndi nzeru zako zonse, ndi mnansi wako monga iwe mwini. Ndipo anati kwa iye, Wayankha bwino; chita ichi, indigo udzakhala ndi moyo.

wako likuchokera, palibe kuti mnansiyo amanena ndani kwenikweni amene mumayenera kumukonda? Kodi ndi munthu wina wake m’mudzi mwathu, kodi ndi mlendo, kodi ndi wina wake ochokera dziko lina, kodi ndi mdani wanga? Mukhoza kukambirana izi kwa ma ola koma osafika kumapeto.

Tsopano takonzeka pa fanizo la Yesu. Kumbukirani, ili ndi yankho la Yesu ku funso lenileni la munthu uja...kodi ndichite chiyani kuti ndipeze moyo wosatha kapena cholowa cha moyo wosatha?

Munthu woyamba kudutsa anali wansembe, chimene chimatanthauza kuti ntchito yake yoyamba inali kupereka nsembe ku kachisi ku Yerusalemu, kumene mwina amapitako. Ngati titati tiyerekeze lerolino, zikhoza kukhala ngati mkulu wa mpingo akupita ku tchalitchi. Malemba amati ngati ukhudza mtembo, kapena thupi lotsala pang’ono kufa, umadetsedwa. Ichi chinali chilamulo. Nthawi zambiri, timaganiza kuti wansembeyu sanasamalire za munthu ovulalayu. Koma iyetu amasunga chilamulo. Komabe, pali vuto. Palinso lamulo lina; limene talitchula pamwambali limene limati, “konda mnansi wako.” Ndiye funso ndi lakuti, kodi lamulo lalikulu ndi liti? Mu chochitika chimenechi, kuti usunge lamulo limodzi, ukuyenera kuphwanya lina. Ngati wansembeyu “amakonda mnansi wake” mkuthandiza munthu ovulalayu, iye waphwanya lamulo lina lija ndipo sangakathenso kukapereka nsembe ku kachisi. Wansembeyu akanakhala odetsedwa ndi kuyenera kubwerera kunyumba ndi kukadziyeretsa komanso kudikira kwa kanthawi asanapite kukapembedzanso.

Choncho, iye wasankha kukhala osadetsedwa. Iye waona kuti lamulo lakuti ukhale osadetsedwa ndi lofunikira kwambiri kuposa kukonda mnansi wako. Kenako, mu Levi akubweranso. Tikhoza kunena kuti Mleviyu anali wapansi pa wansembeyu. Lero, tikhoza kuyerekeza mkulu wa mpingo ndi mtumiki mu mpingo.

Choncho, iye wasankha kukhala osadetsedwa. Iye waona kuti lamulo lakuti ukhale osadetsedwa ndi lofunikira kwambiri kuposa kukonda mnansi wako. Kenako, mu Levi akubweranso. Tikhoza kunena kuti Mleviyu anali wapansi pa wansembeyu. Lero, tikhoza kuyerekeza mkulu wa mpingo ndi mtumiki mu mpingo. Choncho pamene Mleviyu wafika pamalo pamene panali munthu ovulalayu, wachita chimodzimodzi monga wansembe uja. Mwina waganizanso mwa iye yekha kuti kukhala osadetsedwa ndi kofunikira kuposa kukonda mnansi wake. Mwinanso, akudziwa kuti wansembe wake ali patsogolo pake munsewu. Ndipo, iye akunena kwa iye yekha; “ngati wansembe uja sanathandize munthu uyu, ine ndindani kuchita mosemphana ndi munthu amene ali wankulu kwa ine?”

Kenako komaliza pakubwera Msamariya. Tsopano, tizindikire kuti a Yuda ndi a Samariya amadana wina ndi nzake. Pali nkhanu kuchokera mu nthawi ya Yesu pamene mphunzitsi anafunsidwa “Mnansi wanga ndani?” Kodi ndi Myuda amene samapita ku sunagoge mnansi wanga? Kodi ndi msilikari wa Chiroma mnansi wanga? Kodi ndi Msamariya mnansi wanga?” Mphunzitsiyu akuyankha: “Myuda; zikanakhala zabwino akanamapita ku Sunagoge, koma inde iye ndi mnansi wako. Ndipo msilikari wa Chiroma anapangidwanso mchifanizo cha Mulungu, inde, nayenso ndi mnansi wako. Koma Msamariya...iye sanapangidwe mchifanizo cha Mulungu. Ayi, iye simnansi wanga.”

Nkhani imeneyi imatithandizira kumvetsetsa m'mene ubale pakati pa Ayuda ndi a Samariya unalili. Choncho, pamene Yesu akufotokoza nkhanu imeneyi ndipo munthu wachitatu amene akubwera mkukhala Msamariya, aliyense akusinkhasinkha kuti chichitike ndi chiyani. Mwina angomumalizitsa kumupha munthu ovulalayu? Kapena kumulavulira malovu? Koma mukhoza kuganizira m'mene anadabwitsikira pamene Yesu anafotokoza kuti Msamariyayu *anamuthandiza* munthuyu, anamulipirira ndalama, anaika moyo wake pachiopezo pakunyamula Myuda ovulala kulowa naye mumzinda wa Chiyuda ndi kukamuika kumalo ogona alendo. Anthu amene anamuona akumubweretsa Myuda nzawoyu akanatha kumuponya miyala Msamariyayu, pakumuganizira kuti ndi iye amene wamuvulaza.

Tsopano tikufika kumapeto kwa nkhanu. Ndipo kenako Yesu anamuyang'ana katswiri wa chilamuloyu ndi kuti, “Kodi ndani amene anali mnansi wa munthuyu mu nkhanu?” Munthu uja akuyankha, ndipo akuti, “amene anamuthandiza uja.” Udani ndi waukulu kwambiri pakati pa a Yuda ndi a Samariya, kuti mpaka katswiri wa chilamulo uja sakutchula mkomwe mtundu wake wa munthu uja. Mukuona? Iye sakutha kutchula kuti Msamariya. Iye akungoyankha, “Iye amene anamuthandiza uja.” Ndiye onani zimene Yesu wachita. Wapanga “mdani” wa a Yuda kukhala munthu amene akukonda

Mulungu. Iye watenga wina wake amene wina aliyense amavomereza kuti ali kunja kwa ufumu wa Mulungu, kunja kwa mpingo; ndikunena kuti, “Uyu ndi amene wasunga lamulo. Iye wakonda.” Izi ndi zamphamvu.

Mzere omaliza mu nkhanu ukuchokera kwa Yesu; “Pita nuchite iwe chimodzimodzi.” Tikhoza kutanthauzira motere: “Pita, kakonde mnansi wako.” Kumbukirani funso la munthuyu kumayambiriro kuja; “Kodi mnansi wanga ndani?” Ndipo pamene pasanafike, “Kodi ndichite chiyani kuti ndilandire moyo wosatha?” Kodi mukuona yankho la Yesu? Kutu upeze moyo, ukufunikira kukonda mnansi wako. Nanga kodi mnansi wako ndindani? Mnansi wako ndi Msamariya. Mnansi wako ndi mdani wako wamkulu. Choncho kwa ife, Yesu akuti, “Ngati mukufuna kupeza moyo wosatha, mukuyenera kuchita chinachake cha chifundo kwa mdani wako wamkulu.”

Choncho kwa ife, Yesu akuti, “Ngati mukufuna kupeza moyo wosatha, mukuyenera kuchita chinachake cha chifundo kwa mdani wako wamkulu.” Kumbukirani kuti kwa Yesu, moyo wosatha ukuyamba panopa (Yohane. 10:10). Iye akufuna tikhale ndi moyo panopa, osati tsiku lina mtsogolono. Ndipo kodi timapeza moyowu panopa komanso mtsogolo? Kodi timaonetsa bwanji kuti tapulumutsidwa? “Mwa ichi aliyense adzadzwa kuti inu ndinu ophunzira anga ngati mukondana wina ndi mnzake,” (Yohane 13:35). Palibe malamulo ambiri oti adzisungidwa, kapena zokambirana zambiri zoti zidzikhala. “Chikondi,” basi (Onaninso Paulo akufotokoza chimodzimodzi mu a Agalatiya 5:14, 1 Akorinto. 13, and Aroma 13:9-10). Yesu akudziwa kuti iwo amene sangathe kukhululuka panopa, sangakonde panopa, sangakhale ndi mtendere kapena chisangalalo panopa. Kukhalabe mu mkwiyo ndi Kusakhululuka ndi kukhala opanda moyo; ndi kukhala mu gahena panopa (Mateyu. 5:22). Choncho mau omaliza a Yesu ndi kupita ndi kukachita. Sitingakhale ndi kukambirana zakuti kodi mnansi wathu ndani. Sitingamangopita ku malo a mapemphero athu, kusiya maubale osayanjanitsidwa. Yesu akumaliza ndi lamulo kuti uza kuti tipite tikakonde. Chikondi ndiye lamulo lalikulu.

Koma ndindani wa ife amene angakonde chonchi? Nanga munthu uja amene anatipweteka kwambiri, ndizovuta kwa ife ngakhale kutchula dzina lake? Kodi tingamukonde bwanji? Yankho likuyenera kukhala lakuti, zimenezi mwa ife tokha, ndizosatheka. Tikuyenera kuyang'ana kwa Yesu. Yesu ali Pamtanda, pakuona onse iwo amene anamupachika, iye anati, “Atate, akhululukireni.” Tikuyang'ana pa Yesu amene, monga Msamariya uja amene anaika moyo wake pa chiopezo kupulumutsa munthu opweteka, anapereka moyo wake kwa ife. Ndi mphamvu ya Mzimu wa Mulungu mwa ife, pakuona m'mene Yesu anatikondera ife, kutikhululukira ndi kutiyanjanitsa pamene sitinali

oyenera, Ifenso tikhoza kuchitanso chimodzimidzi kwa ena. Ngakhale kwa iwo, amene maina awo sitingathe mkuwatchula komwe.

-Ben Hayes

Kukonda Mulungu Pokonda Anzathu

Ife timakonda Mulungu chifukwa ndi Iye anayamba kutikonda. Ngati wina akanena kuti, “Ine ndimakonda Mulungu” koma namadana ndi m’bale wake ndi wabodza ameneyo. Pakuti aliyense amene sakonda m’bale wake, amene akumuona, sangathe kukonda Mulungu amene sanamuone. Ndipo Iye anatipatsa ife lamulo ili: Aliyense amene akonda Mulungu ayenera kukondanso m’bale wake.

Pakunena za chikondi cha Mulungu ife sitingathe kuchifotokozera kapena kuchimvetsetsa bwino. Mwa chikhalidwe cha dziko lapansi chikondi chimakhalapo pakati pa anthu awiri amene akukhala mwa ubwino ndipo ndi oyanjana. Nthawi zonse amafunirana zabwino.

Pali chikondi chimene chimakhala pakati pa makolo ndi ana awo, pakati pa mwamuna ndi mkazi, pakati pa anthu a pachibale ndiponso pakati pa munthu ndi Mulungu. Ichi ndi chikondi cha uzimu.

Chikondi cheni cheni chimafunika kuti chikhale chochokera ku mbali zonse ziwiri kwa iwo okondanawo. Ngati chingachokere ku mbali imodzi sichichedwa kutha. Wina amapezeka kuti wafooka kapena wakhumudwapo. Komatu siziri chomwecho ndi chikondi cha Mulungu.

Monga mwa lemba lathu la mu 1 Yohane 4: 19 akunena kuti, “Mulungu ndiye anayamba kutikonda”. Pakuyang’ana pa chikondi cha dziko la pansu pamakhaladi wina amene amayamba kukonda komanso pamakhala zifukwa zimene amakopedwa nazo. Okondedwa, muyenera kudziwa kuti Mulungu sanatikonde ife chifukwa kuti tinali abwino ayi, kapena kuti tinali olungama ayi! Palibe chiri chonse Mulungu anangotikonda basi osayang’ananso ngakhale machimo athu.

Pa Masalimo 78: 37 mpaka 40 akunena kuti “Popeza mtima wao sunakonzekera Iye, ndipo sanakhazikika m’chipangano chake. Koma Iye pokhala ngwa chifundo, anakhululukira choipa osawaononga; Nabweza mkwiyo wake kawiri kawiri. Sanautsa ukali wake wonse. Ndipo anakumbukira kuti iwo ndiwo anthu; Mphepo yopita yosabweranso.

Kawiri kawiri nanga anapikisana ndi Iye ku chigwako, namumvetsa chisoni m’chipululu”.

Pa lemba limeneli tikuona kuti mtundu wa anthu sunasiyebe kupikisana ndi Mulungu ndipo nthawi zambiri timakhalabe oukira m’makhalidwe athu. Moyo wobwelera bwelera ku machimo, osafunanso kulapa kumeneko ndiko kumuukira Mulungu. Chikondi ndi khalidwe la Mulungu. Aroma 5:8 akunena motere, “Koma Mulungu anaonetsa chikondi chake kwa ife pa ichi: Pamene tinali chikhalire ochimwa, Khristu anatifera”.

Tikabwelera pang’ono m’mbuyo pa vesi ya 7 akunena kuti “Sizichitika kawiri kawiri kuti munthu wina afere munthu wolungama, ngakhale kuti chifukwa cha munthu wabwino wina atha kulimba mtima kumufera”. Aliyense wa ife titafunsidwa kuti kodi mumakonda Mulungu? Tipereka yankho lonena kuti inde. Timakonda Mulungu bwanji?

Ena akhoza kuyankha mofulumira kuti pakusonkhana ndi anzanga tsiku la mulungu, ena kuthandiza osowa, ena kulakira ndi kufalitsa uthenga wabwino. Zonsezi ndi zofunika ndipo tiyenera kumachita koma sizionetsa kweni kweni kuti tikukondadi Mulungu. Zina mwa zimenezi zikhoza kuchitika koma chikondi pa Mulungu osakhalamo.

Monga mwa mau a Paulo mu 1 Akorinto 13:1 - 13 tikuona za kuposa kwa chikondi. Chikondi chimene Paulo akugawana nafe ndi chikondi cha pakati pa munthu ndi munthu. Chikondi chimenechi ndi chimene chimapangitsa kuti chikondi cha pa Mulungu

1 Johane 4:19-21

Tikonda ife, chifukwa anayamba Iye kutikonda. Munthu akati, kuti, Ndikonda Mulungu, nadana naye mbale wake, ali wabodza: pakuti iye wosakonda mbale wake amene wamuona, sakhoza kukonda Mulungu amene sanamuona. Ndipo lamulo ili tili nala lochokera kwa Ire, kuti iye amene akonda Mulungu akondenso mbale wake.

chitheke ndipo chikhale choona.

Mu mavesi athu amene tikugawana nthawi ino, tikumva Yohane akutilangiza kuti aliyense amene amati akonda Mulungu akondenso m’nansi wake. Kodi zimenezi zimatheka? Kodi tiribe ena mwa iwo otizungulira kuyambira kunyumba kwathu, m’mudzi mwathu, pa gome lathu ngakhale ku dera lathu amene timawaona ngati adani ndipo sitiyanjana nawo? Mulungu, amene alibe tsankhu ndipo Iye amakonda abwino ndi oyipa omwe, akufuna kuti ife tiwonetse chikondi kwa iwo amene timawatcha adani.

“Munamva kuti kuanenedwa, Uzikondana ndi mnansi wako, ndi kumuda mdani wako: Koma Ine ndinena kwa inu, kondanani nawo adani anu, ndi kupempherera iwo akuzunza inu; kotero kuti mukakhale ana a Atate wanu wa kumwamba”; Mateyu 5: 43 – 45. Ngati tingakonde Mulungu zinayenera ziziyamba ndi anansi athu maka maka iwo amene ndi adani athu. Ngati zikukanika kapena sizikutheka ndiye kuti sizingathekenso kumukonda Mulungu.

Ambiri timapezeka kuti ndife abodza chifukwa cha maudani amene akukanika kutha pakati pathu, chikhalirecho ife tikunena kuti timakonda Mulungu ndipo tikutumikira chifukwa cha chikondi chathu pa Mulungu. Kusalolerana, kusamvana ndi makangano pakati pathu zimapangitsa kuti anthu akunja asalandire uthenga wathu ndipo sangapulumuke chifukwa cha ife. Ena tikunena kuti timakonda Mulungu koma m'banja mwathu tinasiya kale kale kuyankhulitsana ndi akazi kapena amuna athu. Ena ngati tingayankhulane mwina zimangotheka potumizirana mauthenga a pa foni basi. Kwa ena, angokhalabe pabanjapo popeza pali ana koma chikondi cha pa banja chinatha kale.

Atsogoleri a pa malo a mpingo sakuyanjana, koma nkumalalikirabe ndi kumanyemetsa mgonero wa Ambuye, nkumati timakonda Mulungu. Amabwelera kwao osakonza ubale wao woonongeka ndipo salapa. Amaumitsabe mtima mwinsano osakhululuka eti chifukwa amakonda Mulungu ndipo akuchita zimene Mulungu akufuna. Bodza lalikulu. Mulungu amangotiseka.

Aliyense amene akonda Mulungu akondenso m'bale wake. Ife timathamangira kukonda Mulungu nkumayesa tikuchita bwino koma Mulunguyo akufuna kuti ngati tingamukonde Iye, tiyambe ndi kuwakonda anansi athu. Si onse amene ali anansi athu omwe ndi anthu abwino. Ena samatifunira zabwino ndipo ena amatinyoza kuti ndife anthu oyipitsitsa. Yesu akufuna kuti tiwakonde otere ndipo tidziwapempherera ndi kuwafunira zabwino osati kuwatemberera. Dziyeseni nokha ngati mumakondadi Mulungu. Kodi ubale wanu ndi anthu ena ndi wotani?

-Symon Katete

Za Chitukuko

Umphawi ndi chinthu chimodzi chimene chimawapangisa anthu kukhala akusakasaka mayankho azinthu zina m'moyo wao. Izi zimachitika chifukwa chofuna kuti miyoyo yao iziyenda bwino. Ngakhale ziri chomwechi alipo anthu ena amangokhala momwe aliri kumati bola ali akhristu zao ziri bwino m'malo molimbikira kugwira ntchito. Chifukwa chamaganizo amenewa, anthu komanso mabanja ambiri amalephera kutukuka. Pokhala ife akhristu tikuyenera kudziwa kuti Mulungu anatipatsa kuthekerera koti tikhoza kupanga malonda ndi ntchito zina ngakhale tili ochepekedwa ndi kumatukula mabanja athu. Lero lino kuli magulu osunga ndi kubwereketsa ndalama amene pa chizungu amati (Village savings and Loans (VSL)), omwe cholinga chao ndi chofuna kutukula miyoyo ya anthu pa chuma.

VSL ndi chidule cha mawu a mchingerezi otchedwa Village savings and Loans. Pologalamu

imeneyi inakhazikitsidwa muchaka cha 2014 mu maboma ochepe. Cholinga cha pologalamuyi ndi kusintha miyoyo ya ma membala a mpingo wa Khristu, m'moyo wa kuthupi komanso ku uzimu kudzera mu magulu akusunga ndi kubwereketsana ndalama.

Pakukhala m'maguluwa, ma membala amasunga ndalama pang'onopang'ono ndi kukhala ndi mwayi wotenga ngongole zoyambira ma bizinesi ang'onoang'ono kudzera mu ndalama zawo zomwezo. Amagawananso mau a Mulungu pa mkumano uliwonse, zimenezi zimathandiza kuti akule mu moyo wawo wa uzimu.

Ubwino wokhala mu maguluwa ndi wankhanikhani monga kukhala ndi mwayi wotenga ngongole zoyambira ma bizinesi pa chiwongola dzanja chaching'ono, kuthandizika pamavuto wogwa mwadzidzidzi, kusunga ndalama iliyonse yomwe wapeza pafupi ndi kuphunzira ma luso osiyanasiyana.

Palinso ntchito zina zomwe maguluwa amayenera kuchita pambali pa kusunga ndi kubwereketsana ndalama. Ntchito zake ndi monga ngati kuthandiza ku mpingo ndi thandizo lomwe angakwanitse komanso kuthandizira kufalitsa uthenga wa bwino, wachikondi kudzera mu kufikira osowa a m'mudzi komanso mu mpingo.

Kudzera mu pologalamuyi, mipingo yina yakwanitsa kukomzanso malo awo osonkhaniranamo. Chitsanzo ndi mpingo wa Khristu wa ku Kasenga m'boma la Rumphu omwe a laliki ake ndi a Felix Mhone. Mpingo wina ndi wa ku Chinkhoma m'boma la Kasungu. Mipingoyi inamanganso malo awo opemphereramo kudzera mu gulu lawo.

Anthu ambiri mu maboma osiyanasiyana apindulanso pokhala ndi ma businesi okhazikika. Padakali pano pologalamuyi iri mu madera ena a m'dziko la Mozambique komanso m'maboma monga Rumphu, Mzimba, Nkhotakota, Kasungu, Machinga, Mulanje, Zomba komanso Phalombe mu Malawi muno.

Anthu ena amakhala ndi maganizo oipa akamva nkhani yokhuza VSL chifukwa cha magulu ena amene amalephera kupita chitsogolo chifukwa choti ma membala ake alephera kubwenza ndalama zomwe anabwereka. Izi zimachitika chifukwa cha magulu oyamba alibe cholinga chofuna kukwaniritsa m'moyo wao ndipo mapeto ake akabwereka ndalama amangodziononga. Ndipo atalephera kubwenza ndalama, zotsatira zake, amaluzi katundu. Zimanezi zimachitika ngati magulu akungoyambitsidwa ndi anthu omwe alibe cholinga china chiri chonse m'moyo mwao. Poona mavuto amene ndi chifukwa chake Namikango Mission inayambisa maphunziro akayendetsedwe ka magulu amenewa ndi cholinga chofuna kuti iwo amene ali okonzeka kukhala ndi kusatira zofunika magulu amenewa akhale ndi mwayi omakumana ndi kumalimbikitsana.

Chiwerengero cha magulu omwe tilinawo padakali pano ndi oposera 164 ndipo ndi malo ochuluka omwe akufuna pologalamuyi itawafikira. Mulungu akugwira ntchito yake yosintha miyoyo ya anthu kudzera mu pologalamuyi.
-Towera Manda

Zolengeza

Maphunziro ku Namikango

Tikufuna kudziwitsa abale ndi alongo m'mipingo yonse ya Khristu kuti tiri ndi ganizo loyambitsa maphunziro atsopano a Baibulo kuno ku Namikango. Maphunzirowa azidzaphunzitsidwa mchingerezi ndipo onse ofuna kudzalowa adzayenera kudzakhalala ndi certificate ya form 4 (MSCE). Ndipo certificate yo iyenera kudzakhalala ndi ma kilediti anayi, imodzi mwa iwo idzakhalale pa phunziro la chingerezi (English). Zonse zikakonzeka tidzatumiza mauthenga kudzera ku mipingo ndi njira zina.

Misonkhano ya misasa

Misonkhano ya misasa ya chaka chino iyamba mwezi wa June motere:

07 – 09 June	Changoima (Chikwawa)
21 - 23 June	Naphazi (Thyolo)
21 - 23 June	Lamusi (Zomba) (Msonkhano wa amayi)
28 - 30 June	Mivumo (Phalombe)

Msonkhano waukulu mu 2020

Monga tonse tikudziwa kuti msonkhano waukulu wa mpingo wa Khristu mu chigawo cha kummwela kwa Africa (SAIL), chaka chino unachitikira dziko la Eswatini (Swaziland). Tithokoze Mulungu abale ndi alongo anayenda bwino. Chaka cha mmawa msokhano onga omwewu ukachitikira ku Bulawayo mu dziko la Zimbabwe. Ndalama yolembetsera ndi R600. Ino ndi nthawi yabwino kuti tiyambe kukonzekera.

Omwe anatisiya

- Gogo Mary Thindwa anatisiya pa 18 February ndipo anaikidwa pa 22. Iwo amasonkhana ndi Mpingo wa Redcross komanso Kachere Church of Christ.
- M'bale Mkhuwawe omwe anali mlaliki mudera la Chingale pa Mpingo wa Ntaka (Zomba), anamwalira pa 20 April, ndipo analowa m'manda pa 21 April, 2019 kwao ku Chingale.
- M'bale Chinseu omwe amasonkhana pa Namilongo church (Zomba) komanso anali mlaliki anamwaliranso pa 20 April, ndipo analowa m'manda pa 21 April, 2019 kwao ku Namilongo.

Kupemphelera odwala ndi achikulire

Tidzikumbikira kupemphelera abale awa:

- Bambo Ephraim Master kwa Mayaka ku Zomba.
- Bambo John Katete ku Chingale m'boma la Zomba.
- Bambo Samson Mbewe ku Liwonde m'boma la Machinga.
- Bambo Bvuta ku Likangala m'boma la Zomba.